THE LANCET
Global Health

## Supplementary appendix 1

This translation in Chichewa was submitted by the authors and we reproduce it as supplied. It has not been peer reviewed. *The Lancet*'s editorial processes have only been applied to the original in English, which should serve as reference for this manuscript.

Kutanthauzila kwa mu Chichewa uku kwachokela kwa alembi a nkhaniyi ndipo tayipeleka kwa inu m'mene tayilandilila. Mawu a mu Chichewa sanawunikilidwenso kapena kukonzedwa. Nkhani ya mu Chingelezi yokha ndi imene yadutsa mu ukonzi wa Lancet, kotelo kuti nkhani ya mu Chingeleziyi ndi imene ikuyimilila mokwanila nkhani yonse imene yalembedwa.

Supplement to: Lawrence DS, Muthoga C, Meya DB, et al. Cost-effectiveness of single, high-dose, liposomal amphotericin regimen for HIV-associated cryptococcal meningitis in five countries in sub-Saharan Africa: an economic analysis of the AMBITION-cm trial. *Lancet Glob Health* 2022; **10:** e1845–54.

Kutanthauzila kwa mu Chichewa uku kwachokela kwa alembi a nkhaniyi ndipo tayipeleka kwa inu m'mene tayilandilila. Mawu a mu Chichewa sanawunikilidwenso kapena kukonzedwa. Nkhani ya mu Chingelezi yokha ndi imene yadutsa mu ukonzi wa *Lancet*, kotelo kuti nkhani ya mu Chingeleziyi ndi imene ikuyimilila mokwanila nkhani yonse imene yalembedwa.

**Kafukufuku wowonkhetsa ndalama zimene zimagwiritsidwa ntchito ndi phindu limene limapezeka popeleka dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B kwa anthu amene ali ndi kachilombo ka HIV amene ali ndi matenda owumitsa khosi a cryptococcal meningitis kum'mwera kwa Africa**

**Chiyambi:** Matenda owumitsa khosi a cryptococcal meningitis ndi matenda amodzi amene amachititsa imfa zambiri za anthu amene ali ndi kachilombo ka HIV. Kafukufuku wa AMBITION wawonetsa kuti kupeleka dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B kuphatikiza ndi mankhwala okumwa pakamwa kumachiza matenda owumitsa khosi a cryptococcal meningitis mofanana ndi ma dilipi asanu ndi awiri a mankhwala a amphotericin B deoxycholate ndipo mankhwalawa amapeleka mavuto ochepa kwa anthu odwala. Apa tikukupatsani zotsatira za kuwonkhetsa ndalama zimene zimagwiritsidwa ntchito ndi phindu limene limapezeka popeleka dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B kumene kunachitika mu mayiko asanu mu Africa muno.

**Kapangidwe ka kafukufuku:** Anthu opitilila ma handrede asanu ndi atatu (814) anatenga nawo mbali mu kafukufukuyu ku mayiko a Botswana, Malawi, South Africa, Uganda ndi Zimbabwe. Tinanyang'ana ndalama zimene zimagwiritsidwa ntchito ndi zipatala mu mayiko osiyanasiyana wa popeleka chithandizo kwa munthu amene akudwala matenda owumitsa

khosi a cryptococcal meningitis kwa masabata khumi, kufaniza amene akulandila dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B ndi amene akulandila ma dlipi asanu ndi awiri a mankhwala a amphotericin B deoxycholate.

**Zotsatira:** Kutenga dziko la Malawi ngati chitsanzo, ndalama zokwana 1369 US dollars zimagwiritsidwa ntchito pa munthu aliyense amene analandila dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B pamene ndalama zokwanila 1237 US dollars zimagwiritsidwa ntchito pa munthu aliyense amene analandila ma dlipi asanu ndi awiri a mankhwala a amphotericin B deoxycholate. Zimafunikila ndalama zowonjezela zokwana 128 US dollars (95%CI;$59-$257) pa moyo wina uliwonse umene unapulumutsidwa ndi dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B. Tikachotsela mtengo wa zinthu zimene zimafunikila chifukwa cha kutenga mbali mu kafukufuku, ndi kuyesezela kuti akulandila chithandizo cha kuchipatala cha nthawi zonse, mtengo wowonjezela wa chisamaliro umatsika kufikila pa 80 US Dollars (95%CI;$15-$275). Zinthu zimene zimasintha kwambiri mtengo wa chisamaliro cha kuchipatala zinali nthawi kapena masiku amene munthu wagonekedwa muchipatala, ndi mtundu wa mankhwala a matenda a cryptococcal meningitis umene walandila. Zotsatirazi zinali zofanana mu mayiko asanu onse ndipo mtengo wowonjezela kuti moyo wa munthu m'modzi upulumuke umayambila 71 US Dollars ku Botswana kufikila 121 US Dollars ku Uganda.

**Tanthauzo la zotsatira:** Kupeleka dilipi limodzi la mulingo wochuluka wa mankhwala a liposomal amphotericin B kunali ndi phindu pa mtengo wawung'ono wowonjezela tikasiyanitsa ndi chithandizo cha ma dilipi asanu ndi awiri a mankhwala a amphotericin B deoxycholate.

Njira imeneyi yopeleka mankhwala a cryptococcal meningitis ithanso kukhala yosowa ndalama zochepela pamene ikugwiritsidwa ntchito kuthandiza anthu mu zipatala zosiyanasiyana zosakhudzana ndi kafukufuku chifukwa cha kuchepa kwa zovuta zimene munthu wolandila mankhwalawa amakumana nazo komanso chifukwa cha kuthekela koti munthu wodwala atha kugonekedwa m'chipatala masiku ochepelako.